

MULUNGU NDI ANTHU

TINGAPULUMUTSIDWE BWANJI KU MACHIMO

TINGAPULUMUTSIDWE BWANJI KU MACHIMO

DON & MARIAN STARKS

Version: Chichewa # 1

MULUNGU NDI ANTHU

TINGAPULUMUTSIDWE BWANJI KU MACHIMO

DON & MATIAN STARKS

Version: Chichewa #1

MULUNGU NDI ANTHU

1. **“Pachiyambi Mulungu**”[Genesis 1:1]

Pachiyambi Mulungu analipo, lero lino alipo ndipo Iye adzakhalabe mpaka nthawi zonse.

2. **Nanga munthu? “Mulungu adalenga munthu...”** [Genesis 1:27]

“.....ndi dothi lapansi, nauzira mpweya wamoyo m’mphuno mwake, munthuyo nakhala wamoyo” [Genesis 2:7]

3. **N’chifukwa chani Mulungu adalenga munthu?**

- Chifukwa cha **ulemelero** wake [Yesaya 43:7]
- Chifukwa cha **ulemu** wake [Chibvumulutso 4:11]

Mulungu analenga munthu ndikumpatsa ufulu osankha kumvera kapena kusamvera. Pachiyambi Mulungu amayankhula maso ndi maso ndi munthu ndipo anamuuza zinthu zomwe angazikonde [Genesis 2:16-17]

4. **Masiku anoso Mulungu amauza munthu chimene chingamusangalatse**

“Koma opanda **chikhulupiriro** sikutheka **kumkondweretsa**; pakuti iye wakudza kwa Iye ayenera kukhulupirira kuti alipo ndi kuti ali obwezera mphototho iwo akumfuna Iye”. [Ahebri 11:6]

5. **Kodi munthu angachipeze bwanji chikhulupirirochi?**

“Chomwecho **chikhulupiriro** chidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa **mau a Mulungu**”. [Aroma 10:17]

BAIBULO

CHIYAMBI CHAKE “Lemba lililonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa

NDI **chiphunzitso, chitsutsano, chikozero, chilangizo** cha m’chilungamo:

CHOLINGA CHAKE kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita **ntchito** **iliyonse yabwino**” [2 Timoteo 3:16-17]

KODI MULUNGU ANATIULULIRA BWANJI MAU AKE?

- “.....anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhura” [2 Petro 1:21]
- “Mulungu anationetsera mau ake mwa Mzimu wake” [1 Akorinto 2:10]

KODI MULUNGU ADAGWIRITSA NTCHITO NDANI NGATI OMUYANKHULIRA?

- “kale Mulungu analankhula ndi **makolo** mwa **aneneri** m’manenedwe ambiri ndi mosiyanasiyana, koma pakutha pake pa masiku ano analankhula ndi ife ndi **Mwana** amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am’mwamba omwe [Ahebri 1:1-2]
1. **Makolo** – Mulungu ankayankhula mwatchutchutchu ndi Abraham, Isake, Yakobo ndi ena ambiri.
 2. **Aneneri** – Mulungu ankayankhula ndi anthu kudzera mwa Mose, Yesaya, Yeremiya, Danieli, Yona, Amosi ndi ena ambiri ndipo analemba m’chipangano chakale zomwe Mulungu anawayankhura.
 3. **Mwana wake** – Mulungu akuyankhula nafe lero mwa Mwana wake kudzera mwa Mzimu Woyera umene anautumiza kuti ukathandizire alembi a chipangano chatsopano.

MUKUKHULUPIRIRA KUTI BAIBULO NDI MAU A MULUNGU?

- EYA – AYI

MAPANGANO AWIRI

MULUNGU ADAPANGANA PANGANO LOPOSERA LIMODZI NDI MUNTHU

1. Pangano loyamba linaperekedwa kwa ana a Israel kudzera mwa Mose (Eksodo 34:27-28)
2. Pangano latsopano linaloseredwa ndi m`neneri Yeremiya (Yeremiya 31:31-34, Ahebri 8:8-12)
3. Mwana wa Mulungu anabwera kudzachotsa pangano loyamba ndi kuika lachiwiri (Ahebri 10:9)
4. M`masiku ano anthu tili mupangano latsopano (2 Akorinto 3:14)
 - Chilamulo cha Khristu (Agalatiya 6:2).
 - Pangano la kale linatha (2 Akorinto 3:14) - Chilamulo cha Mose (Machitidwe 13:39).

MASIKU ANO CHIPANGANO CHA KALE N`CHOFUNIKA BWANJI?

- Aroma 15: 4 Pakuti zonse zinalembedwa kale zinalembedwa kutilangiza, kuti mwa chipiro ndi chithonhozo cha malembo tikhale ndi chiyembekezo.
 - Timaphunzira kuchokera kwa Mulungu m`mene ankachitira ndi anthu a chipangano chakale kuti nthawi zonse amatathauza zimene wanena (Genesis 2:17).

- 1 Akorinto 10:6- Zithu izi zinakhala zitsanzo kwa ife
 - Timaphuzira kuti Mulungu amadalitsa onse amene amvera Iye.

- 1 Akorinto 10:11- Zithu izi zinalembedwa kutichenjeza ife
 - Timaphuzira kuti Mulungu amalanga onse osamvera Iye

Masiku ano tikumangiridwa mu chipangano chatsopano. - Eya - Ayi?

CHIPANGANO CHATSOPANO – CHOTILAMULIRA MASIKU ANO

MULUNGU	Mulungu adapereka kuweruza konse kwa mwana [Yohane 5:22]
↓	
YESU	Yesu adati, “..... mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine kumwamba ndi dziko lapansi.” [Mateyu 28:18]
↓	
MZIMU WOYERA	Yesu adauza ophunzira ake, “..... Mzimu Woyeraadzakuphunzitsani zinthu zonse, nadzakukumbutsani inu zinthu zonse zimene ndidanena kwa inu.” [Yohane 14:48]
↓	
ATUMWI	Ndipo atumwi adati, “.....[Yesu] anatilamulira ife tilalikire kwa anthu, ndipo tichite umboni kuti Uyu ndiye amene aikidwa ndi Mulungu akhale woweruza amoyo ndi akufa.” [Machitidwe 10:42]
↓	
CHIPANGANO CHATSOPANO	Yohane, mtumwi, adalemba , “.....chimene tinachiona, ndipo tidachimva, tikulalikirani inuso..... ndipo izi tilemba ife...” [1 Yohane 1:3-4]
↓	
MUNTHU	Munthu “.....pakuti ife tonse tidzaimirira ku mpando wakuweruza wa Mulungu munthu aliyense wa ife adzadziwerengera mlandu wake kwa Mulungu [Aroma 14:10-12]

CHIPANGANO CHATSOPANO CHIRI NDI ZONSE ZOFUNIKA KUDZIWA LERO - Eya - Ayi

- 2 Petro 1:3 – Mulungu “....idatapatsa ife **zonse** za pamoyo ndi chipembedzo”
- Yohane 20:31 – “koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Khristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m’dzina lake”

BAIBULO – CHOONADI

MULUNGU ADACHENJEZA KUOPSA KOSINTHA MAU AKE

- Chibvumbulutso 22:18-19 – “..... Munthu **akaonjeza** pa awa, adzamuonjezera Mulungu miliri yolembedwa m’bukumu: ndipo ali yense akachotsako pa mau a buku la chinenero ichi, Mulungu adzamchotsera gawo lake pa mtengo wa moyo,”
- Agalatiya 1:8 – “koma ngakhale ife[**atumwi**], kapena **mngelo** wochokera kumwamba [kapena munthu ali yense, v9], akakulalikirani Uthenga Wabwino wosati umene tinakulalikirani inu, akhale wotembereredwa”

MPHOTHY YOTSATIRA UKAKONDA ZINTHU ZINA OSATI MAU A MULUNGU

- Mateyu 15:3 ndi 9 – “inunso mulumphirani lamulo la Mulungu chifukwa cha **miyambo yanu?** koma andilambira ine kwachabe, ndikuphunzitsa **maphunzitsa a anthu.**”
- Akolose 2:8 – “penyani kuti pasakhale wina wakulanda inu ngati chuma, mwa kukonda nzeru kwake, ndi chinyengo chopanda pake, potsata **mwambo wa anthu**, potsata zoyamba za dziko lapansi, osati potsata Khristu”

CHONCHO, TIVOMEREZE BAIBULO NGATI CHINTHU CHOKHACHO CHOTIUZA CHOONADI

Eya - Ayi

- Machitidwe 17:11 – “Amenewa.....**nasanthula** m’malembo masiku wonse, ngati zinthu zinali zotero.....”
- 1 Atesalonika 2:13 – “.....pakulandira **mau a Mulungu**, simunawalandira monga **mau a anthu**, komatu monga **momwe ali** ndithu, **mau a Mulungu.....**”
- Yohane 8:32 – “ndipo mudzazindikira **choonadi**, ndipo **choonadi** chidzakumasulani”

CHOONA CHOKHUDZA CHIPEMBEDZO

1. Kodi ndizipembedzo zochuluka motani zimene ziri m’maderamu?

a. Nanga mudayamba mwadabwapo kuti mipingo ikuchokera kuti?

_____ Eya - Ayi

b. Kodi izi zimakusokonezani ?

Eya - Ayi

c. Nanga kodi ndi Mulungu amene anayambitsa chisokonezochi ? Eya - Ayi

[Taonani 1 Akorinto 14:33]

2. Kodi ndi mipingo ingati imene Mulungu analonjeza kudzakhazika? _____

[Mateyu 16:18]

a. N'chifukwa chani ukutchedwa Mpingo **wake**?

Yankho: chimodzimodzi chifukwa chimene zovala za ine zikukhalira zanga.

- Yesu **adagula mpingo** ndi mwazi wake [Machitidwe 20:28].

b. Kodi **"mpingo"** ndi chani? Ndi nyumba yopemphereramo kapena gulu la anthu?

- "Koma inu [akhristu] ndinu **thupi** la Khristu....." [1 Akorinto 12:27]

c. **"Mpingo"** [mawu a chigiriki ndi **Eklesia**] ndi **oitaniidwa** amene ndi gulu la anthu

[1 Petro 2:9]

1) Kodi nanga Baibulo limanena kuti thupi limeneli ndi chani? _____

[Aefeso 1:22-23]

2) Kodi Baibulo limanena kuti matupiwa alipo angati? _____

[Aefeso 4:4]

3) Kodi Baibulo pamenepa likunena za mipingo ingati? _____

d. Kodi Yesu Khristu ndi mutu wa matupi [mipingo] angati ? _____

[Aefeso 5:23]

3. Kodi mipatuko yonseyi idachokera kuti? Kwa Mulungu kapena munthu.

a. Buku la Machitidwe 20:30 limanena kuti " ndipo mwa inu nokha adzauka anthu oyankhula zokhotakhota [molekana ndi choonadi] kupatutsa ena awatsate"

b. 1 Timoteo 4:1 "pakuti idzafika nthawi imene sadzalora chiphunzitso cholamitsa, koma monga mwa zilakolako za iwo okha..... Ndipo makutu awo sadzamvera choonadi..... "

4. Kodi mipatuko yonseyi adayivomereza ndi Mulungu?

a. "Koma ndikudandaulirani inu, abale, mwa dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu, kuti nonse **munene chimodzimodzi**, ndipo kuti **pasakhale malekano** pakati panu, koma **mumangike mu mtima umodzi womwewo** ndi **m'chiweruzo chomwecho**" [1 Akorinto 1:10]

b. Kodi ndikuyenera kukhala mu mipatuko?

Eya -Ayi

5. Yesu amafuna ophunzira ake akhale amodzi




- a. Pakuti sindipempherera iwo okha komaso iwo akukhulupirira Ine chifukwa cha mawu awo kuti onse akakhale amodzi kuti dziko lapansi likakhulupirire kuti Inu munandituma Ine (Yohane 17:20-21)
- b. Kodi ophunzira/otsatira Yesu angakhale bwanji amodzi?
 1. Osasamala nthano zachabe za chiyuda ndi malamulo a anthu opatuka kusiyana nacho choonadi (Tito 1:14)
 2. Pasakhale wina wakulanda inu ngati chuma mwa kukonda nzeru kwaKe ndi chinyengo chopanda pake potsata mwambo wa anthu, potsata zoyamba za dziko lapansi osati potsata Khristu (Akolose 2:8)
 3. Wonani (1 Akorinto 1:10) m`mwambamu
Onse akugwiritsa ntchito mawu a choonadi mofanana (Yohane 17:17)

6. Mawu a Mulungu amatiuza za mpingo umodzi

- a. Kodi mukugwirizana nazo kuti Yesu ali ndi mpingo wake umodzi? Eya -Ayi
- b. Kodi tikuyenera tonse tikhale mu mpingo umodzi umenewu? Eya -Ayi

ZOONA ZOKHUDZA CHIPULUMUTSO

1. Pachiyambi (Genesis 2:16-17)
 - a. Mulungu anampatsa munthu mwayi osakha
 - Kumvera, (Zoti adye)
 - Kusamvera, (Zoti asadye)
 - b. Mulungu adamuza munthu zotsatira za kumvera kapena kusamvera
 - Moyo (Kuyanjana naye)
 - Imfa (Kulekana naye)
2. Pamene munthu anasakha kusamvera analekana naye Mulungu
 - Yesaya 59:2 Koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu, ndipo machimo anu abisa khope Yake kwa inu kuti lye sakumva
 - Yakobo 1:15- Tchimo.... limabala imfa
 - Genesis 3:22-24



ZOCHITA ZA MUNTHU

ZOTSATIRA ZAKE


- Aroma 6:23a- pakuti photho ya uchimo ndi **imfa.....**”
 - Yakobo 2:10- “.... Koma akakhumudwa palimodzi.....**wachimwira** onse.”
 - Aefeso 2:12- “... popanda Yesu.....**palibepo chiyembekezo.....**”
 - Aroma 8:7- “....chisamaliro cha thupi **chidana** ndi Mulungu...”
 - Yesaya 59:2- “.....**zakulekanitsani** inu ndi Mulungu wanu.....”
 - 1 Akorinto 6:9- “....**osalungama** sakalandira.....”
- Imfa**
kuchimwa
- kulowerera**
udani
kulekanitsa
kusalungama

ZOONA ZOKHUDZA CHIPULUMUTSO

1. Mulungu anali ndi dongosolo

- Aefeso 1:9-10 “....Cholinga cha Mulungu.....kuti pa makozedwe a makwaniridwe a nyengozo , akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Khristu”

2. Dongosolo la Mulungu poyanjanitsaso (ubale) lye ndi anthu



- 2 Akorinto 5:19- “...Mulungu anali mwa Khristu alikuyanjanitsa dziko lapansi kwa lye yekha.....”
- Aroma 5:10- “... Tinayanjanitsidwa ndi Mulungu mwa imfa ya Mwana wake...”

Uthenga wabwino

Chilango chimene chinaperekedwa Aroma 5:8-
Kulungamitsidwa Aroma 5:9a-
Kupulumutsidwa Aroma 5:9b

Kuyanjanitsidwa Aroma 5:10-

Tonse pamodzi Aroma 5:11-
Kulungamitsidwa Aroma 5:19-

Chifundo cha Mulungu

“...Khristu **anatifera.**”

....**Tinalungamitsidwa** ndi mwazi wake

“...**Tinapuluma** ku mkwiyo mwa lyeyo”

“...**Tinayanjanitsidwa**(kukozanso ubale) mwa imfa ya Mwana wake”

“...Talandira **chiyanjano**”

“...Ndi kumvera kwa m`modzi ambiri adzayesedwa **olungama**”

UCHIMO - BVUTO LA MUNTHU

1. Mphotho ya uchimo ndi imfa” Aroma 6:23a

- Mphotho ndi phindu, cholowa, kapena chithu chomwe chimalipiridwa.

2. Kodi tchimo ndi chiyani?

- Chosalungama** chiri chose ndi tchimo....”(1 Yohane 5:17, onani Aroma 1:29-32;Agalatiya 5:19-21; 1Akorinto 6:9-10)
- Aroma 14:23-“... chithu chonse **chosatuluka m`chikhulupiriro** ndicho uchimo.”
- Yakobo 4:17”... amene adziwa **kuchita bwino ndipo sachita** kwa iye kuli tchimo.”
- 1 Yohane 3:4-“...Yense wakuchita tchimo **achita kusaweruzika...**”


Pamene tikulephera kufikira pa mulingo wa Mulungu ndiye kuti tikuchimwa

3. Bvuto

Munthu amayesera kuthana ndi mvuto la kulekana ndi Mulungu koma-

“.....**Njira ya anthu** sili mwa iye mwini.... Kulongosola mapazi ake.”
(Yeremiya 10:23; onani Yesaya 55:8-9)

“ Pakuti onse anachimwa **naperewera** pa ulemerero wa Mulungu,” (Aroma 3:23)



4. Chilango

- Mateyu 25:41 ndi 46- chokani kwa Ine.....kumoto wa nthawi zonse wokozedwera mdyerekezi ndi amithenga ake..... ndipo amenewa adzachoka kunka ku chilango cha nthawi zonse.....

CHIKONDI- NJIRA YA MULUNGU

1. “...Mphotho ya Mulungu ndiyo moyo wasatha wa mwa Khristu Yesu Ambuye wathu”
(Aroma 6:23b)

- Mphatso ndi chosapindula, chosatiyenera, chosalipira, choperekedwa mwa chikondi

2. Mtengo - Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kutero kuti **anapatsa** mwana wake obadwa yekha...(Yohane 3:16)


- Levitiko 17:11- ..Pakuti wachita chotetezera ndiwo mwazi(pamodzi ndi Mulungu)

chifukwa cha moyo wake

- b. Aheberi 9:22 - "...Popanda kukhetsa **mwazi** palibe kukhululukidwa kwa machimo"
- c. Aroma 5:8 - Mulungu atsimikiza kwa ife **chikondi** chake cha mwini yekha m`menemo..... **Khristu adafera** ife."

3. Yesu adalipira mtengo omwe ife sitikadawanitsa kulipira

- a. 1 Yohane 2:2-.. Ndipo iye ndiye chiwombolo/dipo la machimo athu...
- b. 1 Petro 2:24 Amene anaseza machimo athu mwini yekha mthupi mwake pa mtanda.



4. N`chifukwa chiyani mwazi wa Khristu

- a. Mwazi wa nyama sunkachotsa machimo (Ahebri 10:4-5)
- b. Mwazi wa ochimwitsitsa, munthu okhudzidwa sangaperekere mtengo wa machimo wa mzake.

chitsanzo; monga akupha awiri aweruzidwa kuti apedwe m`modzi sangafe m`malo mwa winayo. Onse ndiwo okhudzidwa, onse akuyenera kulipira, onse akuyenera afe

- c. "Pakuti Khristunso adava zowawa kamodzi chifukwa cha machimo, **olungama m`malo mwa osalumgama**, kuti akafikitse kwa Mulungu **ophedwatu** m`thupi...."

(1 Petro 3:18)

MPHATSO YA MULUNGU (YESU + MOYO) MUNTHU AYENERA KULANDIRA

Ine ndi **njira** choonadi ndi moyo
Palibe munthu adza kwa Atate koma
Kwa Ine (Yohane 14:6)

Iye amene akaniza Ine ndi **kusalandira mau anga** ali naye omuweruza iye mau amene ndalankhula ndi inu iwowa Adzamuweruza tsiku lomaliza (Yohane12:18)

MAU A YESU

Kumva (Yohane 5:24)

"Iye wakumva mau anga ndi kukhulupirira Iye amene anandituma Ine ali nawo moyo wosatha"

+ akuyenera kuchita **osangova** kokha (mateyu 7:24)

Kukhulupirira (Yohane 8:24)

" ...ngati **simukhulupirira** kuti Ine ndine mudzafa m`machimo anu"

+ akuyenera kuchita osati kungokhulupirira

kokha (Yakobo 2:19, Yohane 12:42)

Kuvomereza (Mateyu 10:32) “ ...Yense amene **adzavomereza** Ine pamaso pa anthu

Inenso **ndidzamvomereza** iye pamaso pa Atate wanga
Wa kumwamba”

+ akuyenera kuchita ntchito osati **kungvomereza** kokha
(Aroma 10:9-10)

Kulapa (Luka 13:3)

“ ...koma ngati **simutembenuka** mtima mudzaonongeka
nonse momwemo”

+ akuyenera kuchita ntchito osati **kulapa** kokha
(Machitidwe 2:38)

Kubatizidwa (Marko 16:16)

“ Amene akhulupirira **nabatizidwa** adzapulumutsidwa”

+ akuyenera kuchita ntchito **osangobatizidwa** ayi
(Machitidwe 8:38)

Kukhala okhulupirika

(Chibvumbulutso 2:10)

“**Khala wokhulupirika** kufikira imfa ndipo ndidzakupatsa
iwe korona wa moyo”

+ kuchita osangokhala **okhulupirika**.

MAYAKHO A ZOYANKHULA ZA YESU

Yesu anauza ophunzira ake kuti, “mukani ku dziko lonse la pansi lalikirani **Uthenga Wabwino** (imfa, kuikidwa m`manda, kuuka- 1 Akorinto 15:1-4) kwa olengedwa onse.
Amene **akhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa** koma amene sakhulupirira
adzalangidwa (Marko 16:16)

ZOTSATIRA ZAKE ZINALI ZOTANI PAMENE ATUMWI ANACHITA MONGA MOMWE YESU
ANAWALAMULIRA?

AYUDA PA TSIKU LA PENTEKOSITE “**atamva ichi (Uthenga wabwino)** analaswa mtima
(Machitidwe 2:37-47) (**kukhulupirira**), nati....tidzachita chiyani amuna inu

Abale? koma Petro anati... **lapani, batizidwani** yense wa inu m`dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu.....pamenepo iwo amene **analandira** mau ake **anabatizidwa** tsiku lomwelo ndipo Mulungu / Ambuye anawonjezera tsiku ndi tsiku amene akuti **apulumutsidwe.**”

ASAMALIYA(Mach 8:5-21)

“...Filipo... anawalikira Khristu (**Uthenga wabwino**)... ndipo pamene **anakhulupirira** zimene Filipo anawaphuzitsa zokhudzana ndi ufumu wa Mulungu ndi dzina la Yesu, onse amuna ndi akazi **anabatizidwa.**”

MDINDO (Mach 8:35-39)

“ Filipo... analalikira Yesu (**Uthenga wabwino**)... mdindoyo anati, taona apo **madzi** chindiletsa nchani kuti ndibatizidwe? Filipo anati, ngati ukhulupirira Yesu ndi mtima wako wonse , ukhoza.....Iye.....anati ndikhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu.....onse Filipo ndi mdindo anatsikira ku madzi ndi **kubatizidwa** iye.....anapita njira yake **wokondwera.**”

ONANI MOMWE ANTHUWA ANAYANKHIRA ATALALIKIDWA UTHENGA WABWINO

___Anamva___anakhulupirira___analapa___anamvomereza___anabatizidwa___anapulumuka

ZOONA ZENIZENI ZA KULAPA

1. **Kulapa** ndi “.... Kutembenuka...” (kusiya zoipa- Machitidwe 3:19)

Mwachitsanzo:

a. Machitidwe 8:27-“..... Mdindo..... anadza ku Yerusalemu kudzapembedza.”

(Apa padali munthu amene adasintha chipembedzo chake.)

b. Machitidwe 9:6-“... Ambuye, amafuna ndichite chiyani?

(Nthawi yomweyo Paulo anazindikira kuti anali Yesu , ndipo adasintha maganizo ake)

c. Machitidwe 16:33- Mdindo wa ndende anakhudzika “ndipo anawatsuka mikwingwirima yawo.”

(Apa padali munthu amene adasintha zochita zake)

d. Machitidwe 19:18-19 - kusintha kwa anthu awa kudawapangitsa kuti awononge zinthu zoipa zomwe adali nazo.

2. kodi mwaona kuti ndi **nthawi yaitali bwanji** imene anthu awa adatenga **kuti alape**.
 - a. Machitidwe 2: 38 ndi 41- Ayuda adamvera lamulo pa tsiku la pentekosite “tsiku lomwero.”
 - b. Machitidwe 16:33- Wandende adasitha “ora lomwelo la usiku”
3. **Kulapa** ndiko kudzipereka(Aroma 12:1-2; 1 Petro 4:1-2)
 - a. **Kusintha** njira ya moyo wako (osadzifanizira ndi makhalidwe apansi pano)
 - b. **Kusintha** kaganizidwe (“ pokozedwanso maganizo” ndi mawu a Mulungu).
 - c. **Kusintha** kuchoka kumakhalidwe ako kupita kwa Mulungu.

ZOONA ZA KUVOMEREZA

1. **Osati** “kuvomereza machimo” koma “kuvomereza Yesu Ambuye ndi pakamwa pako.” (Aroma 10:9)
2. **Osati** “kungopemphera mkudutsa”; **osati** kungopemphera kuti machimo akhululukidwe - Pemphero la chikhulukiro lisungidwira ana a Mulungu. (1 Yohane 1:9; 1 Petro 3:12)
3. **Anati**: “Ndikhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu” (Machitidwe 8:37; 1 Yohane 4:15)
4. **Kuonetsa** ndi moyo wanga (“pamaso pa anthu”- Mateyu 10:32) Kuti ndimamutsatira lye (Luke 9:23)

ZOONA ZENIZENI ZA UBATIZO

1. **Ubatizo** ndiko **kumiza m`madzi**
 - a. Machitidwe 8:38 –“ndipo onse awiri anapita **kumadzi** Filipino ndi mdindo ndipo anabatizidwa mdindoyo.”
 - b. Aroma 6:4-“...**Tinaikidwa m`manda** pamodzi ndi lye mwa ubatizo kulowa mu imfa yake...”
2. **Chipulumutso** chimabwera **pamene wabatizidwa**
 - a. Marko 16:16- “Amene akhulupirira nabatizidwa **adzapulumutsidwa...**”
 - b. Machitidwe 2:38-“ Lapani, **ndi...** kubatizidwa... **kuloza** kuchikhulukiro cha machimo anu...”
 - c. Machitidwe 22:16-“...Tauka nubatizidwe, **ndi kusamba kuchotsa** machimo ako...”
3. Amene **adabatizidwa** adali **akulu msikhu**.
 - a. Machitidwe 8:37-“...Ngati wakhulupirira ndi mtima onse, ukhoza.....ndipo anayakha nati.....(munthu ayenera kukhulupirira, kuvomereza ndi pakamwa pake - Aroma 10:9).
 - b. Kodi mwana angave ndi kuvetsa mau a Mulungu? Kukhulupirira, kulapa, kuyankhula?**
4. Amene anatembunuka anabatizidwa **nthawi yomweyo**

- a. Machitidwe 2:41, "...Iwo amene analandira mau ake anabatizidwa... tsiku lomwelo..."
- b. Machitidwe 16:33- "...Ora lomwelo la usiku... apabanja ake onse anabatizidwa."

5. Kuphunzira zambiri kumabwera **pamene wabatizidwa**

- a. Yesu anati, "pitani...phunzitsani...ndi kuwabatiza... kuwaphunzitsa asunge..." (Mateyu 28:19-20)
- b. Machitidwe 2:41-47- "...iwo amene anabatizidwa...anali chikhalire m`chiphunzitso cha Atumwi ndi mchijanano, mkunyema mkate, ndi mapemphero... Ndipo Mulungu anawaonjezera ku mpingo tsiku ndi tsiku amene akuti **apulumutsidwe.**"

KODI UBATIZO NDIWOFUNIKA BWANJI?

1. UBATIZO KOMASO MTANDA WA KHRISTU SIZINGALEKANITSIDWE

- Ngati mgonero (chiyanjano) wa Ambuye zikusiyantsidwa ndi imfa ya Yesu ndiye kuti ziribe tathauzo.


(Mgonero wa Ambuye = Thupi ndi Mwazi umene Yesu anakhetsa pa mtanda

- Mateyu 26:26-28)

- Ngati **ubatizo** zingalekanitsidwe ndi imfa ya Yesu ndiye kuti ziribe tathauzo. (Ubatizo = **imfa + kuikidwa m`manda + kuuka m`manda** kwa Yesu -Aroma 6:3-4)

- Aroma 6:3-4—"Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Khristu **tinabatizidwa mu imfa yake?** Chifukwa chake **tinaikidwa m`manda** pamodzi ndi lye mwa ubatizo kulowa mu imfa, kuti monga Khristu **anaukitsidwa** kwa akufa mwa ulemmerero wa Atate, chotero tikayende m`moyo watsopano."

2. SUNGALEKANITSE UBATIZO NDI MWAZI WA YESU



Ubwino wa mwazi wa Yesu → **ndidalandira liti?**

- Mateyu 26:28 - **kuchotsa machimo**

batizidwani kuloza ku "chikhululukiro cha machimo" - Machitidwe 2:38

- Ahebri 9:14 - **kuyeretsa chikumbumtima**

ubatizo ndi “yankho la chikumbumtima chabwino”

-1 Petro 3:21

- Chivumbulutso 1:5- **kuchotsa machimo**

batizidwa ndi kusamba “**kuchotsa machimo**” -

Machitidwe 22:16.

CHONCHO SITINGALEKANITSE UBATIZO NDI CHIPULUMUTSO.

KUMVERA UTHENGA WABWINO

- 2 Atesalonika 1:7-8 “..... Pa bvumbulutso la Ambuye wochokera kumwamba pamodzi ndi angelo a mphanvu yake, m’lawi lamoto, ndi kubwezera chilango kwa **iwo osamvera Uthenga Wabwino** wa Ambuye wathu Yesu”
- **Kodi Uthenga Wabwino ndi chiyani?**
 - a. Yesu **adafa** chifukwa cha zochimwa zathu - 1 Akorinto 15:1-4
 - b. Yesu **adaikidwa m’manda**
 - c. Yesu **adauka** - [1 Atesalonika 4:14]

UTHENGA WABWINO NDI KUFA, KUIKIDWA M’MANDA, NDI KUUKA KWA KHRITSU

- **Ndi chiyani chomwe ndingachite kuti ndionetse kuti ndikumvera Uthenga Wabwino?**
Aroma 6:3-4 – “kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Khristu Yesu; tinabatizidwa mu **imfa** yake? Chifukwa chake **tinaikidwa** m’manda pamodzi ndi lye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Khristu **anaukitsidwa** kwa akufa mwa ulemerero wa Atate, chotero ifenso tikayende m’moyo watsopano.”

MU UBATIZO TIMAZINDIKIRA IMFA, KUIKIDWA, NDI KUUKA

Choncho ife, “**timabadwa mwatsopano**”. [Yohane 3:3]


- 2 Akorinto 5:17 – “chifukwa chake ngati munthu ali yense **ali mwa Khristu** ali **wolengedwa mwatsopano**: zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano.”

Kodi munachita zimenezi [**kufa, kuikidwa manda ndi kuuka**]? {Aroma 6:17}

Kodi inu muli mwa Khristu?

CHIFUKWA CHIYANI MWA KHRISTU?

“Potero ngati aliyense ali mwa **Khristu**, ali cholengedwa cha tsopano; zakale zapita/zatha ; choncho zithu zonse zakhala za tsopano. Tsopano chiri chonse ndi cha Mulungu amene adatiyanjanitsa kwa lye mwa Khristu Yesu ndipo adatipatsa utumiki wa **chiyanjanitso**.. Mulungu anali **mwa Khristu** alikuyanjanitsa dziko lapansi kwa lye yekha , osawerengera zolakwa zao.....Pakuti lye (Mulungu) adapanga lye amene sadadziwe **tchimo**, koma ife kukhala ochimwa, kuti tikakhale olungama a Mulungu **mwa lye**. (2 Akorinto 5:17-21).



- Aroma 6:3 - “.. Ife tonse amene tinabatizidwa mwa Khristu Yesu....”
- Agalatiya 3:27- “....Pakuti nonse amene munabatizidwa kwa Khristu mudavala Khristu”

**KODI KUNJA KWA MPINGO WA KHRISTU KULISO MADALITSO AUZIMU?
EYA - AYI**

MAFUNSO

1. Kodi munthu akhoza kupulumuka ngati sali mwa Khristu? Eya- ayi?
 - a. Kodi mudali **mwa Khristu** musanabatizidwe? Eya- Ayi?
 - b. Kodi **mudali opulumutsidwa** pamene mudali musanabatizidwe? Eya- Ayi?
2. **Kodi muli okozeka kudzaweruzidwa ndi mau a Yesu?** Eya- Ayi?
3. Kodi **munakhulupirira Uthenga Wabwino** mongaso **adachitira ena** m`baibulo? Eya- Ayi?

-Kodi munabatizidwa ndi ubatizo **omiza** (Aroma 6:4; Akolose 2:12;) **m`madzi** (Machitidwe 8:38-39)? Eya -Ayi?
4. Kodi **munabatizidwa** pa **zifukwa zofanana** ndi amene ali mu Baibulo? Eya -Ayi?
 - a. Kodi ubatizo wanu “udali okhulukidwa machimo” (Machitidwe 2:38) “kubatizidwa ndi kusamba kuchotsa machimo ako” (Machitidwe 22:16) Eya- Ayi?

(Kodi munthu waphunzira molakwika akhoza kubatizidwa molondola? – ngati anaphunzira kuti wapulumutsidwa asanabatizidwe ndiye kuti abatizidwa pa cholinga cholakwika)
 - b. Ngati munabatizidwa ndi **cholinga cholakwika** muyenera kubatizidwaso (Machitidwe 19:1 -7)? Eya- Ayi?
5. **Kodi muli okozeka** kubatizidwanso mu **njira yoyenerera** ndi **cholinga choyenera**? Eya- Ayi?
 - a. Atamva, kukhulupirira, kuvomereza ndi kulapa, kodi padatenga nthawi yaitali bwanji m`Baibulo asanabatizidwe?

Machitidwe 2:42_____Machitidwe 8:36_____Machitidwe 16:33.
 - b. **Kodi muli okozeka tsopano** (2 Akorinto 6:2) kuti mubatizidwe kusamba kuchotsa machimo anu? Eya- Ayi?

CHOTSATIRA N’CHIYANI UKATHA UBATIZO?

1. **Ndinu olengedwa mwatsopano** [2 Akorinto 5:17] **obadwa mwatsopano**
 - a. “Monga ana obadwa kumene, akhumba mkaka oyenera.....” [1 Petro 2:2]
 - b. Siyani “.... tayani zoipa zonse..... chinyaso.....maonekedwe onyenga.... Kaduka.... masinjiriro [1 Petro 2:1]
 - c. Kulani“.....mchikhulupiriro.....ukoma.....chizindikiritso.....chodziletsa.....chipiriro..... chipembedzo.....chikondi cha pa abale..... chikondi” [2 Petro 1:5-7]

2. **Kuphunzira**

2 Timoteo 2:15

a. “.....okonzeka kuchita chodzikanira.... Pachikhulupiriro chimene chiri mwa inu.....”
[1 Petro 3:15]

b. “..... kuti akaphunzitse ena” [2 Timoteo 2:2]

3. **Tikondane wina ndi mzake** [Yohane 13:34]

4. **Kuchita ntchito zabwino** [Mateyu 5:16, Aefeso 2:10, Agalatiya 6:10]

5. **Khala okhulupirika kufikira imfa**(ngakhale mutafa ndi chikhulupiriro chanu) [Chibv 2:10]

6. **Nthawi imene mkhristu wachimwa**

a. muli ndiNkhoswe (m'khala pakati) wa Atate, ndiye Yesu Khristu.....” [1 Yohane 2:1]

b. mumayenera muvomereze

1) “ngati tibvomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye,kuti atikhululukire machimo athu, ndikutisambitsa kutichotsera machimo, ndi chosalungama chiri chonse [1 yohane 1:9]

2) amene ali ndi mwayi umenewu mndani?

a. amene ali ndi kuthekera pa mwazi wa Yesu umene utisambitsa

b. kwa amene ali ndikuthekera pa Mulungu pokhala mwa Khristu [Aefeso 2:18: 3:12]

c. **Mukuyenera kulapa komaso kupemphera:** chitsanzo [Machitidwe 8:22]

d. mkhristu akhale odekha. Werengani 1 Yohane 5:14-15

7. **Kusonkhana ndi akhristu** [Ahebri 10:25]

a. **Liti?** Tsiku loyamba la sabata ankasonkhana [machitidwe 20:7]

b. **chifukwa chani?:** kupembedza Mulungu mu mzimu ndi mchoonadi [Yohane 4:24]

1) kulalikira ndi kuphunzitsa [machitidwe 20:7]

2) m'gonero wa Ambuye [1 Akorinto 11:23-29; Mat 26:26-29; Mach 20:7]

3) kupemphera [1 Akorinto 14:15; 1 Atesalonika 5:17]

4) kuimba zotamanda Mulungu [1 Akorinto 15:15; Aefeso 5:19; Akolose 3:16]

5) kupereka [1 Akorinto 16:1-2; 2 Akorinto 9:6-7]

DZIWANI IZI: Kupembedza kumene sikuli muuzimu ndi mchoonadi ndikwachabe [Mateyu 15:8-9]

c. **Ndikuti?**, nanga ndi ndani? Iwo amene ali ndi chikhulupiriro chantengo wapatali [2 Petro 1:1]

1) **mpingo** umene **yesu ndiye mutu** [Aefeso 1:22]

2) **mpingo** umene **mamembala ake** amatchedwa kuti akhristu machitidwe 11:26, overa mtima[Afilipi 1:1, Ana a Mulungu 1 Yohane 3:1-2, Ansembe 1Petro 2:5,9,

3) **mpingo** umene **umalemekeza** dzina la mwini wake amene anaumanga [mateyu 16:18]

a. ” Mpingo wa Mulungu” - 1 Akorinto 1:2; Mach 20:28

b. ” thupi la Khristu” - Akolose 1:18; Aefeso 1:23

c. ”mkwatibwi wa Yesu” - Aroma 7:4; Chibv 21:9

d. ”Nyumba ya Mulungu ” - 1 Timoteo 3:15

e. ” Mpingo wa Khristu ” - Aroma 16:16

f. ”mpingo ” - Machitidwe 2:47, Aefeso 5:24-25

KODI MPINGO WA KHRISTU NDI CHIYANI?

- Mpingo wa Khristu umapangidwa ndi anthu amudziko lino lapansi amene amakumana/kusokhana pamodzi ndi cholinga chopembedza Mulungu. Anthu ena amasokhana ochepa m`chiwerengero chawo, ena amakwana mpaka chikwi (1,000) komanso kupitirira apo m`chiwerengero chawo akamapembedza.

1. DZINA

Timadzitchula kuti “Akhristu” chifukwa chakuti tinadzipereka kwa Khristu ndi kubwezeretsa mpingo wake wa m`chipangano chatsopano.

Mau akuti mpingo wa Khristu amangoonetsa umwini. Osati kukhala ndi dzina lina loposa dzina lakuti Mpingo wa Khristu (m`chitidwe umene unakanizidwa mu

(1 Akorinto 1:10-13) tikupempha kuti pakhale mgwirizano potsatira chiphunzitso cha Yesu (Yohane 17:20-21) komaso cha atumwi (Aefeso 2:20)

2. LAMULO LA CHIKHULUPIRO KOMANSO MAKHALIDWE

Mgwirizano wa chiphunzitso ndi makhalidwe zimakondweretsa chifukwa cha kuvomereza Khristu kuti ndi “wamphamvu zonse” (Mateyu 28:18)

Paja chikhulupiro chimadza pakumva mau a Mulungu (Aroma 10:17) ndiye tisachirikizike pa luntha lathu (Miyambo 3:5) apa tikupeza kuti chiri chonse chimene sichinalamuliridwe ndi mau a Mulungu sichiri choyenera kwa Mulungu.

Ife tikuyenera kuchotsa chiphunzitso komanso makhalidwe amene sakupezeka **m`mau** a Mulungu (Chivumbulutso 22:18-19)

3. DONGOSOLO LA MPINGO

Khristu ali **mutu** wa **Mpingo** (Aefeso 1:22), Mpingowu ulibe likulu padziko lino la pansi. Mpingo wa Khristu uli onse wapamalo umakhala odzilamulira komanso woima pa okha. Oyang`anira pa mpingo amasankhidwa kutengera zoyenera zomwe timazipeza pa buku la 1 Timoteyo 3:1-13 komanso Tito 1:5-9. Ndipo amatumikira monga m`mene lanenera buku la 1 Petro 5:1-4.

4. KAPEMBEDZEDWE KAKE

Popembedza, timatengera ndondomeko monga m`mene Yesu ananenera (Yohane 4:24) kuti “Mulungu ndiye mzimu ndipo opembedza/kumlambira lye ayenera kulambira mumzimu

ndi m`choonadi”. Mumzimu ndi kuchokera mumtima, m`choonadi ndi kuchokera mu ulamuliro wa mau a Mulungu. Mpingo umene unalembedwa mu m`chipangano chatsopano umapanga magawo asanu a kupembedza; Kulalikirira (chiphunzitso cha atumwi machitidwe 2:42), Kudya mgonero wa Ambuye (kunyema mkate), Kuimba, Kupemphera, chopereka. Tiri ndi chitsanzo pamene mpingo unabwera pamodzi kunyema mkate (Machitidwe 20:7) komanso kutenga chopereka kwa okhulupirira (1 Akorinto 16:1-2) pa tsiku loyamba la sabata, la mulungu.

5. KUKHALA MKHRISTU

Onse amene timawerenga m`chipangano chatsopano, amene anamvera lamulo la Ambuye limene lye ananena kwa atumwi (Marko 16:15-16), amaonjezedwa ku mpingo ndi Ambuye (Machitidwe 2:47). Lero lino akhristu alibe ulamuliro ofuna zambiri kapena zochepera kuchokera kwa amene akufuna kukhala mwana wa Mulungu zosiyana ndi zimene tingawerenge m`chipangano chatsopano.

6. CHOLINGA

Monga Yesu anatuma ophunzira ake ku dziko lonse lapansi kuti akalalikire Uthenga Wabwino (Mateyu 28:18-20), ifenso timazindikira kuti ndi udindo wathu kulalikirira uthenga kwa olengedwa onse kuti onse akhale ndi mwayi olandira madalitso amene Yesu anakwaniritsa ndi imfa yake pamtanda.

MUKUITANIDWA KUTI MUDZIWE CHOONADI CHOKHUDZA CHIPEMBEDZO KOMANSO KUKHALA MKHRISTU, MUKHOZANSO KUWERENGA IZI MU BAIBULO.

KODI INUYO MWASANKHA NJIRA ITI?

Ya Mulungu kapena ya anthu?

1. Kodi pali chiri chonse m’phunziro ili chimene simunachikhulupirire kuti ndi choonadi? Eya-Ayi
2. Kodi pali chiri chonse m’phunziro ili chimene simunamvetse? Eya-Ayi
3. Kodi pali chiri chonse m’phunziro ili chimene simukugwirizana nacho? Eya-Ayi
4. Kodi ndikanakhala kuti ndinakuphunzitsani kuchokera mumabuku azipembedzo za mpatuko ndipo inu mudasankha kutsatira, kodi zidakakupangani kukhala ndani? Mkhristu - Ena
5. Ngati mwasankha kutsatira chiphunzitso cha m’chipangano chatsopano, kodi zikukupangani kukhala ndani? Mkhristu- Ayi
6. Nanga ndi nthawi iti imene mukuyenera kuchita Uthenga Wabwino? Tsopano – Nthawi ina
7. M’chifukwa chiyani simukuyenera kucedwa popanga chisankho?

a. Yakobo 4:13-17 – “.....simudziwa chimene chidzagwa mawa.....”

b. 2 Petro 3:9-12 – “..... Ambuye..... aleza mtima.....wosafuna kuti ena aonongeke koma kuti onse afike kukulapa. Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala”

KODI MUDZAKHALA OKONZEKA ?

EYA -- AYI

c. 2 Atesalonika 1:7-10 – Ngati **simunamvere Uthenga Wabwino, kodi ndinu okonzeka?**

Eya-Ayi

8. Kodi tsopano ndinu okonzeka kuchita zimene mau a Mulungu akunena?

Eya - Ayi

MAFUNSO

ENA

AYANKHIDWA

KODI NDI CHIPANGANO(LAMULO) CHITI CHIMENE TIKHALAMO LERO?.....Tsamba 22-24

NANGA WAKUBA UJA PA MTANDA?.....Tsamba 25

KODI NDI NTHAWI ITI IMENE MUNTHU AMAKHALA OCHIMWA?.....Tsamba 26

KODI ZOZIZWA ZINATHA?.....Tsamba 27-28

KODI MUNTHU OPULUMUTSIDWA AKHOZA KUGWA KUCHISOMO.....Tsamba 28-29

KODI MUNTHU AKHOZA KUPEMBEDZA MULUNGU MOYENERA POGWIRITSA NTCHITO NYIMBO ZA ZIDA.....Tsamba 29-30

KODI NDI CHIPANGANO(LAMULO) CHITI CHIMENE TIKHALAMO LERO?

CHAKALE(Ahebri 8:13)

KAPENA

CHATSOPANO(Ahebri 8:13; 9:15)

Chidaperekedwa kwa ana a Israeli okha
(Deut 5:1-3; 1 Mafumu 8:9)

chidaperekedwa kwa anthu a mitundu yonse
(Ahebri 8:13)

Chidaperekedwa kudzera kwa Mose (Eks 34:27)	chidaperekedwa kudzera kwa Yesu Khristu (Ahebri 9:15)
Zimaperekedwa mwa mwazi wa zinyama (Ahebri 9:18-19)	chidaperekedwa ndi mwazi wa Yesu Khristu (Ahebri 9:12)
Chidaperekedwa mwa kanthawi kochepe (Ahebri 10:3)	chidaperekedwa mpaka kalekale (Ahebri 10:12)
Sichimachotsa machimo (Ahebri 10:11)	chidachotsa machimo onse (Ahebri 10:12)
Chidatha ndithu (2 Akorinto 3:11,14; Akolose 2:14)	sichidzathanso (2 Akorinto 3:11)
Chidapita (2 Akorinto 3:11)	chikadalipo (2 Akorinto 3:11)

1. Kodi ndi chifukwa chiyani chipangano choyamba (Ahebri 9:1) chinaperekedwa? (Agal 3:19 ndi 24)

2. Kodi kuchotsedwa kwa chipangano chakale kukuphatikizanso ndi malamulo khumi aja?

2 Akorinto 3:7-15 – “...zolembedwa pamwalazidapita.”

Ahebri 9:1-4 – “..... zoikika za kulambira.....ndi magome a chipangano”

Aroma 7:6-7 – “.....tinamasulidwa kuchilamulo usasirire.”

Aefeso 2:15 – “atachotsa.....mau a chilamulo.....”

3. Kodi sitiri omangidwa kuti tizisunga malamulo khumi a Mulungu? (Aroma 8:12)

a. Malamulo khumi opezeka m’chipangano chatsopano

1 – Aefeso 4:6

5 – Aefeso 6:1

8 – Aefeso 4:28

2 – 1 Akorinto 10:14

6 – 1 Yohane 3:15

9 – Akolose 3:9

3 – Yakobo 5:12

7 – Ahebri 13:4

10 – Akolose 3:5

b. umboni wina (Mateyu 22:36-40; Aroma 13:8-9)

Yesu anati: “Ndikupatsani inu **lamulo latsopano.....kuti mukondane wina ndi mnzake.....**”(Yohane 13:14)

4. Nanga za lamulo losunga tsiku la sabata?

a. Chinali chizindikiro pakati pa Mulungu ndi ana a Israeli okha (Eks 31:16-17) **Ndani? – Israeli**

b. Chinali kuti azikumbukira kuombedwa kuchokera ku ukapolo (Deut 5:15) **chifukwa chani? – chikumbukiro**

c. A mitundu **sanali pansi pa chilamulo**(Aroma 2:14)

- onani Machitidwe 15 – dziwani kuti **sadalamulidwe** kuti “azisunga tsiku lasabata.”

5. N’chifukwa chiyani akhristu amapembedza Mulungu pa tsiku loyamba la sabata?

a. Yesu adauka kwa akufa **tsiku loyamba la sabata** (Marko 16:1-9)

b. Kuonekera koyamba kwa ophunzira atasonkhana kunali **tsiku loyamba la sabata** (Yohane 20:19)

c. Kuonekeranso m’masiku makumi anayi(40) kunali **tsiku loyamba la sabata** (Yohane 20:16)

d. Mzimu Woyera unafika **tsiku loyamba la sabata** (Machitidwe 2)

e. Ulaliki woyamba wa Uthenga Wabwino udalalikidwa **tsiku loyamba la sabata** (Machitidwe 2)

f. Ophunzira amasonkhana **tsiku loyamba la sabata** kunyema mkate (Machitidwe 20:7)

g. Chopereka chimatoleredwa **tsiku loyamba la sabata**(1 Akorinto 16:2)

h. Mtumwi Yohane, analitenga ngati tsiku lopambana – **Tsiku la Ambuye**(Chibvumbulutso1:10)

i. **Mupangano latsopano** muli m’ndandanda wa **zinthu zatsopano** zochititsa chidwi

1) **Dzina** latsopano (Yesaya 62:2; Machitidwe 4:12; 11:26)

2) **Gulu** latsopano – **mpingo** (Daniel 2:44; Machitidwe 2:47)

3) **Chiphunzitso** chatsopano – **Uthenga Wabwino** (Yesaya 2:3; Luka 24:47)

4) **Lamulo** latsopano – **chikondi** (Yohane 13:34)

5) **Unsembe** watsopano (Ahebri 7:24-28)

6) **chikumbukiro** chatsopano – **M’gonero wa Ambuye** (Mateyu 26:26-29)

7) **Tsiku** latsopano – **tsiku la Ambuye** (Chibvumbulutso 1:10)

6. Chenjezo:

Akolose 2:16 – “.....munthu ali yense asakuweruzeni inu kapena.....tsiku la **Sabata**,”
Agalatiya 5:4 – “.....inu amene muyesedwa olungama ndi lamulo ; mudagwa posiyana nacho chisomo.” Werengani

2 Akorinto 3:14-16 – ndi maganizo andani amene anachititsidwa khungu? Ndi mitima yandani imene inaumitsidwa?

NANGA WAKUBA UJA PAMTANDA

1. Kodi adapulumutsidwa?

a. Eya, Yesu adamuza iye “.....lero lino udzakhala ndi ine m’paradaizo.”

(Luka 23:43)

b. Yesu anali ndi mphamvu zonse kuphatikiza kutikhululukira machimo athu pamene Iye anali pano padziko lapansi
(chikhulupiriro chomwe anthu amakhala nacho Marko 2:5-12, ana a Abraham Luka 19:7-10, chikhulupiriro cha munthu payekha Luka 7:48-50, opanda chifukwa Yohane 8:3-11)

c. Choncho palibe chitsanzo chokhululukira pamene Yesu asadafe chimene chingakhale chitsanzo chatu lero lino.

2. Kodi ndi nthawi iti yomwe wakubayo adakhululukidwa machimo?

a. Pamene Iye asanafe pamtanda paja, choncho lamulo la Mose linali likugwira ntchito(Akolose2:14)

b. Pamene Yesu anali asanamalize kupereka nsembe ya machimo a anthu padziko lapansi
(Ahebri 9:12)

c. Pamene Uthenga Wabwino unali usanakwaniritsidwe(imfa, kuikidwa m’manda , kuuka – 1 Akorinto 15:1-4)

d. Pamene Yesu anali asanapereke lamulo lake kwa anthu lolalikira za imfa yake ndi Uthenga Wabwino(Marko 116:15,16; Mateyu 28:18 - 20)

e. Pamene pangano latsopano linali lisanakhazikitsidwe (Ahebri 9:16-17)

f. Pamene Uthenga Wabwino wachipulumutso unali usanalalikidwe (Machitidwe 2)

3. Mathero

a. Wakuba uja sanakabatizidwa kuchotsa machimo chifukwa magazi a Yesu anali asanakhetsedwe; Yesu anali “asanafe machimo athu.”

(Aroma 5:8)

b. Mbala ija sinakachita “**Uthenga Wabwino**” chifukwa imfa, kuikidwa m’manda ndi kuuka zinali zisanachitike.

c. Izi sizoonika kwa iwo **okhala patali ndi mtanda.**

KODI NDI NTHAWI ITI IMENE MUNTHU AMAKHALA WOCHIMWA?

1. Kodi munthu amabadwa muuchimo?

- Masalimo 51:5 - “Onani, ndinabadwa m’mphulupulu: Ndipo mai anga anandilandira m’zoipa” - Chimene Davide anatengera mwa makolo ake ndi kufooka kwa thupi pa tchimo (Onani Aroma 7:18). Sanabadwe ndi machimo a makolo ake.
- Ezekiel 18:20 – “Moyo wochimwawo ndiwo udzafa; mwana sadzasenza mphulupulu za atate ake, ndi atate sadzasenza mphulupulu za mwana; chilungamo cha wolungama chidzakhalira, ndi choipa cha woipa chidzakhalira” - Munthu sabadwa ndi tchimo. Aliyense amalandira chilungo potengera ndi zimene iye mwini wachita.

2. Kodi ndi nthawi iti imene munthu amakhala wochimwa?

a. Nthawi imene amakhala wamkulu imene akhonza **kudziwa** njira ya Mulungu:

- Yakobo 4:17 – “..... iye amene **adziwa** kuchita bwino ndipo sachita
- Aroma 14:23 – “.....chinthu chiri chonse chosatuluka m’chikhulupiro, ndicho uchimo.” - Aroma 10:17

b. Pamene ali wamkulu oti akhoza **kuchita** tchimo; ndipo kuti, kusirira ndi kugonjera zilakolako:

- Yakobo 1:15 – “.....pamenepo chilakolako chitaima, chibala uchimo;..... imfa”
1 Yohane 3:4 - “Yense wakuchita tchimo achitanso kusaweruzika

c. Nthawi imene munthu amakhala wamkulu ndipo akhoza **kusankha** njira ya Mulungu kapena ya anthu:

- Aroma 6:16 – “.....mudzipereka eni nokha..... uchimo.... Kapena kumvera

3. Nanga ana ang’ono ?

Yesu anati:

“Lolani tiana tidze kwa Ine.....pakuti Ufumu wa Mulungu uli wa totere.” (Marko 10:14)

“Ngati simutembenuka mtima, nimukhala monga tianato (osalakwa), simudzalowa konse mu Ufumu Wa kumwamba.” (Mateyu 18:3-4)

KODI ZOZIZWITSA ZINATHA?

1. Cholinga cha zozizwitsa – kutsikimizira choonadi

- a. Mose anayankhula choonadi cha Mulungu ndipo anatsikimizira ndi zozizwitsa(Eksodo 4:1-9, 29,30)
- b. zozizwitsa za Yesu zinali zotsikimizira umwana wake wopatulika.
(Mateyu 11:2-5; Yohane 20:30-31)
- c. Atumwi anapatsidwa mphamvu yochita zozizwitsa kuti “...akatsikimizire mau a Mulungu”
(Marko 16:17-20)

Choonadi chinatsikimiziridwa – Ahebri 2:3-4

2. Mphamvu yochita zozizwitsa – mphatso za Mzimu Woyera.

- a. Kulandiridwa ndi ubatizo wa Mzimu Woyera(Machitidwe 1:5; 2:4,43; 11:16-18)
 - 1) Ubatizo wa Mzimu Woyera sunalamuliridwe ndiposo sunali “wochotsa machimo”
 - 2) **Lero kuli ubatizo umodzi** (Aefeso 4:5), **ubatizo wa m’madzi**(1 Petro 3:20-21)
- b. Imalandiridwa munthu akasanjikidwa manja ndi atumwi
(Machitidwe 8:14-18; 19:1-7; 2 Akorinto 12:12)
- 1 Akorinto 12 pali mdandanda wa “mphatso za Mzimu Woyera”
1 Akorinto 13 ananenapo “ kusalika kwa nthawi ya mphatsozi”

Mphamvu zinatha – Atumwi onse anafa – “ koma pamene changwiro(**mau**) chafika tsono chamderamdera(mphatso) chidzakhala chabe”

(1 Akorinto 13:10)

3. Zozizwa Zinatha

- a. Zozizwitsa za m’Baibulo zinali zenizeni (Zauzimu)
 - 1) Kuyankhula malilime achilendo
(ziyankhulo zosaphunzira. Machitidwe 2:4-8; 1 Akorinto 14:19)
 - 2) Chilengedwe chinasintha
(Mateyu 8:26; 14:15-21; 17:27; 21:19; marko 6:48-50; Machitidwe 13:11)
 - 3) Odwala amachiritsidwa pomwepo (Mateyu 4:24; 8:3; 8:14-15; Machitidwe 5:5:12-15)
 - 4) Opunduka miyendo ndi a khungu, anachira kwathunthu
(Yohane 9:1-25; Luka 7:22; Mateyu 15:31; Machitidwe 20:9-12)

5) Akufa anauka

(Lazaro- Yohane 11; Dorika- machitidwe 9:36-43; Utiko- Machitidwe 20-9-12)

b. Zozwitsa zonga izi sizikuchitika lero lino

1) Polephera kuchita “zozizwitsa” “wochiza” amanena kuti zikuonetsera kusowa kwa **chikhulupiro** (onani Marko 2:3-5 –anzathu anali ndi **chikhulupiro**; Mateyu 17:20-21 ochiza analibe chikhulupiro)

2) Iwo amene amanena kuti amachita “zozizwitsa” lero lino ndi abodza (Onani Marko Marko 16:18 – Yesu anati njoka ndi chiphe “**sikadzawapweteka**”)

Chenjerani ndi aphunzitsi onama ndi ochiza abodza (2 Atesalonika 2:9-12; 1 yohane 4:1)

KODI MUNTHU ATAPULUMUKA AKHOZA KUGWA KU CHISOMO?

1. Machenjezo okhudzana ndi kugwa alipo ochuluka.

- 1 Akorinto 10:12 – “.....iye wakuyesa ali chilili ayang’anire kuti **angagwe**.”
- Agalatiya 5:1-4 – “.....musakodweso ndi goli..... inu amene muyesedwa olungama ndi chilamulo.....**mudagwa posiyana nacho chisomo**”
- Ahebri 3:12- “Tapenyani, abale, kuti kapena ukakhale mwa wina wa inu mtima woipa wosakhulupira, **wakulekana** ndi Mulungu wamoyo;”
- Ahebri 3:14- “pakuti takhala ife olandirana ndi Khristu, **ngatitu** tigwiritsa kuchigwira kufikira chitsiriziro...”
- Ahebri 6:4-6- “pakuti sikutheka.....koma **anagwa** mchisokero, kuwakoza”
- Ahebri 10:26- “pakuti tikachimwa ife eni ake, **titatha** kulandira chidziwitso cha choonadi,..’
- Ahebri 10:38- “..... ndipo ngati **abwerera**, moyo wanga ulibe kukondwera mwa iye”
- Yakobo 5:19- “Abale anga ngati wina wa inu asochera **posiyana** ndi choonadi..... ”
- 2 Petro 1:10- “..... pakuti mukachita ichi **simudzakhumudwa**”
- 2 Petro 2:20-22- “pakuti ngati adatha kuthawa **akodwaso** nanzo, **nangonjetsedwa**, zotsatira zao zidzaipa koposa zoyanbazo. Pakuti pakadakhala bwino kwa iwo akadakhala osazindikira njira..... ndi.... **Kubwerera**.....(monga) galu wabwerera kumasanzi ake ”
- 2 Petro 3: 17- “chenjerani kuti..... **mungagwe kusiya** chikhazikiko chanu...”

2. Zitsanzo za omwe anachitapo

- a. Hananiya ndi Safira(Machitidwe 5:1-11) akhiristu onsewa, anaonongedwa ndi Mulungu ponama ndikuyesera kunyenga mpingo.
- b. Simoni wanyanga(Machitidwe 8:13-23) “anakhulupirira nabatizidwa” (ndiko kupulumuka-Marko 16:16) koma anabwerera “ndikugwidwa ndi zolakwa” chifukwa anayesera kugula mphatso za Mzimu Woyera ndi ndalama.

KODI MUNTHU ANGAPEMBEDZE MULUNGU KOYENERA PAKUGWIRITSA NTCHITO ZIDA ZOIMBIRA NYIMBO?

1. Ngati ndi choncho, kukanakhala kopanda ulamuliro wa chipangano chatsopano (lamulo lachindunji kapena chitsanzo)
 - a. Mulungu analamulira kuyimba kokha mchipangano chatsopano
(1 Akorinto 14:15; Aefeso 5:19; Akolose 3:16)
 - b. Zitsanzo za nyimbo muchipangano chatsopano ndikuyimba nyimbo zamatamando
(Mateyu 26:30; Machitidwe 16:25; Yakobo 5:13; Aroma 15:9; Ahebri 2:12)
2. Mu mbiri, zida zoyimbira sizinkagwiritsidwa ntchito popembedza Mulungu mnthawi ya chikhristu kufikira mu zaka za 600 A.D. Ndiyeno nthawi yakugawanikana pakati pa mipatuko ya Greek Orthodox ndi Katolika. Atsogoleri amene anafuna kukonza mpingo, John Calvin(Presbyterian), John Wesley(Methodist) ndi Charles Spurgeon(baptist) anatsutsa nyimbo za zida chifukwa cha kusapezeka kwake mu mchipangano chatsopano.
3. Kodi Mulungu sanavomereze nyimbo za zida mu chipangano chakale?
 - a. Eya - (2 Samuel 6:5; 2 Mbiri 7:6; Masalimo 98)
Ngakhaleso kulamulira izi (2 Mbiri 29:25)
 - b. Kumbukiraniso; chipangano chakale sichomwe chimatitsogolera(ulamuliro) lero lino.
4. Kodi chipangano chatsopano chinaletsa kugwiritsa ntchito zida zoyimbira?
 - a. Ayi, koma izi sizikupereka chilolezo kwa ife kuzigwiritsa ntchito.
 - b. Sikuti ndife omasuka kuchita chiri chonse chimene Ambuye sanaletse
(monga madzi a lalanje[orange juice] ndi keke pa m’gonero)
5. Kodi zimenezi zimakhala nako kusiyana **kwakukulu** pakupembedza?
 - a. Chitsanzo: mu Levitiko 10:1-2 ana a Aroni anapereka moto womwe sunalamulidwe kwa Ambuye zomwe ndizotsutsana ndi lamulo lake.Moto unatuluka kwa Ambuye ndikuononga iwo

1) Amkalambira Mulungu

- Mulungu sanalamulire **zomwe** anachita
- Pokhala kuti Mulungu sanalamulire izi, Iye sanazilandire
- Ndipo iwo **adafa**

2) Nkhani izi zimakhala zitsanzo kwa ife (1 Akorinto 10:11)

b. Tikamapembedza Mulungu **monga momwe takondera** chimatchedwa **“chipembedzo chozipangira”** (Akolose 2:22-23)

c. Pamene tirambira Mulungu monga mwa miyambo kapena malamulo a anthu, Yesu wati izi **“mzachabe”** (Mateyu 15:3,9)